## PHUNZIRO LA 14

1. Kodi Adamu ndi Hava anachita chiyani atamulakwira Mulungu?
-Anazipangira okha zovala za masamba.

2. Kodi chifukwa chiyani Adamu ndi Hava anazipangira okha zovala za masamba?
-Chifukwa chakuti amkayesayesa kubisa tchimo lawo.

3. Kodi pali amene angathe kubisa tchimo lake kwa Mulungu?
-Palibe.

-Palibe amene angathe kubisa tchimo lake kwa Mulungu.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anazikana zovala za masamba zimene Adamu ndi Hava anazipangira okha?
-Mulungu anazikana zovala za mazambazo chifukwa chakuti amkafuna kumphunzitsa Adamu ndi Hava kuti palibe chimene iwo angachite kuti akhale oloredwa kwa Mulungu.

5. Kodi tingazipange tokha kukhala oloredwa kwa Mulungu chifukwa cha zovala zimene tavala?
-Iyayi.

6. Kodi tingazipange tokha kukhala aloredwa kwa Mulungu chifukwa cha ntchito zathu zabwino?
-Iyayi.

7. Kodi ndi ndani yekha amene anali oyenera kumupanga Adamu ndi Hava kukhala oloredwa kwa Mulungu?
-Mulungu.

8. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anapha nyama ndi kupanga zovala za Adamu ndi Hava?
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava.

9. Kodi Mulungu amkamuphunzitsa chiyani Adamu ndi Hava?
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti kusamvere kumabweretsa imfa.
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti tchimo limabweretsa imfa.
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti chilan-go cha tchimo ndi imfa.

10. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupangira Adamu ndi Hava zovala?
-Chifukwa chakuti Mulungu anamukonda Adamu ndi Hava.

11. -Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanamulole Adamu ndi Hava kuti avale okha zovalazo?
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti ndi Mulungu yekha amene angathe kuwaveka anthu.
-Mulungu amkamuphunzitsa Adamu ndi Hava kuti sadzaŵalola anthu amene amatsata njira zawo.

12. Kodi Mulungu anapanga chiyani kuti Adamu ndi Hava asadzabwererenso ku munda wa Edeni?
-Mulungu anayika mngelo ndi lupanga la moto pa chipata choloŵera m'munda wa Edeni.

-Kodi chinachitika chiyani kwa Adamu ndi Hava, Mulungu ataŵatulutsa m'munda wa Edeni?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:1



-Anakakhala kuti Kayini walima mu mthaka, sibwenzi atakolora china chili chonse.
-Kayini anali oyendayenda pa dziko la pasi.

-Chifukwa chakuti kayini anamumvera Satana mmalo momumvera Mulungu, Mulungu anamuthamangitsa Kayini.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:16

16-Chomcho Kayini anachoka pa maso pa Mulungu ndikukakhala ku dziko la Nodi, kuvuma kwa Edeni.

-Kayini anakana kumumvera Mulungu.
-Chomcho, Mulungu anamuthamangitsa Kayini.

-Kayini anakananso kulapa machimo ake.
-Chomcho, Mulungu anamuthamangitsa Kayini.

-Kenako, Kayini atamwalira, anapita ku chilango chosatha.

-Ndikupusa kukana kumumvera Mulungu.
-Ndikupusa kukana kulapa machimo.

-Musakhale ngati Kayini.

-Kayini anakana kuganiza zakuti iye anabadwira m'machimo.
-Kayini anakana kuganiza zakuti machimo ake ayenera kulandira chilango cha imfa.
-Kayini sanatsate njira ya Mulungu.
-Kayini anatsata njira yake, ndipo anapita ku chilango cho-satha..

funso limeneli?

-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti Kayini avo-
mereze kuchimwa kwake.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti Kayini avo-
mereze kuti iye sanamumvere Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti kayini avo-
mereze kuti iye wamumvera Satana.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhula Mulungu kwa Kayini?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:10-12

10-Ambuye Mulungu anamufunsaso kuti, "Kodi chimene wachitachi ndi chiyani? Magazi a mng'ono wako akundililira Ine kuchokera mu mthaka.
11-Tsopano iwe uli wotembereredwa. Siwudzalimanso pa mthaka imene magazi amng'ono wako alowapo, amene wakhetsa ndi manja ako pomupha.
12-Ukamalima mbewu, mthakayo siyidzakupatsa zokolola zina zilizonse. Ndiponso udzakhala munthu ongoyendayenda, osowa pokhala pa dziko la pasi."

-Kodi Mulungu anapereka chilango pa tchimo la Kayini?
-Inde.

-Mulungu amapereka chilango pa machimo onse.
-Palibe tchimo lina lililonse limene Mulungu samalipatsa chilango.

-Kodi Mulungu anapereka chilango chotani pa tchimo la Kayini?

-Mulungu anamutemberera Kayini.



1-Adamu anakhala pamodzi ndi mkazi wake Hava, ndipo anatenga pathupi, ndipo anabereka mwana wa mamuna, ndipo iye anati, "Ndi chithandizo cha Mulungu, ndalandira mwana wa mamuna." Chomcho mwanayo anamutcha Kayini.

-Mulungu atamutulutsa Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni, Hava anabereka mwana wa mamuna.

-Hava anamutcha mwana wawo woyambayo kuti kayini.

-Kodi chifukwa chiyani Haya analankhula kuti anabereka mwana wake wa mamunayo ndi thandizo lochokera kwa Ambuye Mulungu?

-Chifukwa chakuti Hava amkadziŵa kuti Mulungu ndi amene amapereka moyo.

-Kodi ndi ndani yekha amene amapereka moyo kwa anthu onse?
-Mulungu.

-Mulungu yekha ndi amene amapereka moyo kwa anthu onse.
-Mulungu yekha ndi amene anapereka moyo kwa inunso.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:2

2-Kenako, [Hava] anaberekanso mwana wa mamuna dzina lake Abele.

-Kenako, Hava anaberekanso mwana wa mamuna wachiŵiri.
-Hava anamutcha mwana wake wa mamuna wachiŵiriyo dzina lake Abele.

-Kodi Kayini ndi Abele anabadwira kuti?
-Kunja kwa munda wa Edeni.

-Kodi chifukwa chiyani Kayini ndi Abele anabadwira kunja kwa munda wa Edeni?

-Chifukwa chakuti bambo awo, Adamu, ndi mayi awo, Hava, anamulakwira ndiponso sanamumvere Mulungu, chomcho Mulungu anaŵatulutsa m'munda mwa Edeni.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anatulutsidwa m'munda mwa Edeni, ana awo anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava amkakhala kunja kwa munda wa Edeni, ana awo anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.

-Apa pali chitsanzo:

-Kodi ngati makolo anu ali a Chiyao, inunso mungabadwe wa Chiyao?
-Inde.

-Kodi ngati makolo anu ali akuda, inunso mungabadwe akuda?
-Inde.

-Kodi ngati makolo anu ali azungu, inunso mungabadwe azungu?

-Chifukwa chakuti Mulungu anamutulutsa Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni, Kayini ndi Abele anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.



-Kodi Kayini anamumvera ndani?
-Anamumvera Satana.

-Satana amkafuna kuti Adamu ndi Hava afe.
-Satana amkafuna kuti Kayini amuphe Abele.
-Satana amadana ndi anthu onse.
-Satana akufuna kuti anthu onse afe.
-Satana akufuna kuwapha anthu onse.
-Satana anamuwuza Kayini kuti amuphe Abele mng'ono wake, ndipo Kayini anamumvera Satana.

-Kayini anamumvera Satana, ngati mmene Adamu ndi Hava anamumverera Satana.

-Kodi Mulungu anamuwuza chiyani kayini atatha kumupha Abele, mng'ono wake?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:9

9-Ambuye Mulungu anamufunsa kayini, "Kodi mng'ono wako Abele, ali kuti?" Kayini anayankha, "Sindikudziwa, kodi ndi ntchito yanga yomuyang'anira mng'ono wanga?"

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamufunsa Kayini funso limeneli?
-Kodi Mulungu anadziwa kuti Kayini wamupha Abele?
-Inde.

-Mulungu ali palipose, ndipo amaziwona ndi kuzidziwa zinthu zonse.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamufunsa Kayini

6-Kenako Ambuye anamufunsa Kayini, “Kodi chifukwa chiyani uli okwiya? Kodi chifukwa chiyaninso nkhope yako yili yakugwa?

7-Unakachita zabwino, ndinakakondwera nawe. Koma chifukwa chakuti wachita zoyipa, tchimo lakukhalira pa khomo ngati chirombo cholusa. Likulakalaka kuti likugwere, koma iweyo uligonjetse tchimolo.”

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu analankhulana ndi Kayini, Mulungu atakana msembe ya Kayiniyo?

-Chifukwa chakuti Mulungu amkamukonda kayini.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti kayini alape tchimo lake.

-Mulungu amkafuna kumuthandiza Kayini kuti adziwe kuti sanakatha kupita kwa Mulungu mu njira yake.

-Mulungu amkafuna kumuthandiza Kayini kuti adewe kuti anakatha kupita kwa Mulungu mu njira ya Mulungu yekha.

-Mulungu amkafuna kuti amuthandize Kayini kuti asafe mu Nyanja ya Moto Wosatha.

-Kodi Kayini anamumvera Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:8

8-Tsiku lina Kayini anati kwa mng’ono wake Abele, “Tiye tikayende ku munda.” Atangopita kwawokha, Kayini anamuwukira mng’ono wakeyo ndi kumupha.

-Kodi Kayini anamumvera Mulungu?
-Iyayi.



-Chifukwa chakuti Mulungu anamutulutsa Adamu ndi Hava m’munda mwa Edeni, anthu onse anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.

-Kayini ndi Abele anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.
-Anthu onse anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.

-Kunja kwa munda wa Edeni kuli matenda.
-Kunja kwa munda wa Edeni kuli kudana.
-Kunja kwa munda wa Edeni kuli uchimo.
-Kunja kwa munda wa Edeni kuli imfa.

-Anthu onse anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.
-Anthu onse anabadwira m’matenda.
-Anthu onse anabadwira mu chidani.
-Anthu onse anabadwira mu uchimo.
-Anthu onse anabadwira m’matenda.

-Anthu onse anabadwa ali osiyana ndi Mulungu.
-Anthu onse anabadwa ali akapolo a Satana.
-Anthu onse anabadwa ndi Satana ngati ambuye awo.

-Kodi chifukwa chiyani anthu onse anabadwa ndi Satana ngati ambuye awo?

-Chifukwa chakuti bambo athu, Adamu, sanamumvere Mulungu ndipo anachimwa.
-Chifukwa chakuti bambo athu, Adamu anamumvera Satana.

-Apa pali chitsanzo:

-Tiyelekeze kuti pali adani anu a mtundu wina wake umene ukufuna kupha anthu onse a mtundu wanu.

-Tsiku lina, mwana wa mtundu wanu akupita kwa adani anu aja, ndi kukakwatira mwana wa adani anuwo ndi ku-khala ngati wa mtundu omwewo.

-Kodi ngati iye akubereka ana, anawo adzakhala a mtundu wanji?
-Mtundu wa adani anuwo.

-Chifukwa chakuti bambo athu , Adamu, anamumvera Satana ndikukhala kapolo wa Satanayo, anthu onse anabadwa ngati akapolo a Satana.

-Chifukwa chakuti bambo athu, Adamu, anamumvera Satana ndipo Satanayo anali mbuye wawo, anthu onse anabadwa ndi Satana ngati mbuye wawo.

-Tsiku lina Kayini ndi Abele anafika ndi msembe kwa Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:3

3-Patapita nthaŵi, Kayini anatenga zipatso zina za ku munda, ndikukazipereka ngati msembe kwa Ambuye.

-Kodi Kayini anabwera ndi chiyani ngati msembe kwa Mulungu?
-Kayini anabwera ndi zipatso zina za ku munda ngati msembe kwa Mulungu.

-Kodi Abele anabwera ndi chiyani ngati msembe kwa Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:4a



chilango cha imfa.

-Kodi Kayini amkaganiza chiyani za Mulungu?

-Kayini samkaganiza zakuti Mulungu ndi oyera.
-Kayini samkaganiza zakuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Kayini samkaganiza zakuti Mulungu yekha ndi amene an-gathe kumpulumutsa iye.

-Kayini samkaganizanso zakuti iye akufunika Mpulumutsi kuti ampulumutse iye ku tchimo lake.

-Chifukwa chakuti kayini sanamumvere Mulungu, Mulungu sanalandire msembe ya Kayini.

-Kodi mukukumbukira chifukwa chimene Mulungu anaka-nira zovala za masamba zimene Adamu ndi Hava anazi-pangira okha?

-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti Adamu ndi Hava adziwe kuti panalibe china chilichonse chimene iwowo anakachita kuti adzipange olandiridwa kwa Mulun-gu.

-Mulungu amkafunanso kuti Kayini adziwe kuti panalibe china chilichonse chimene iye anakachita kuti adzipange olandiridwa kwa Mulungu.

-Kodi Mulungu anati chiyani kwa Kayini, Iye atayikana msembe ya Kayini?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:6-7

-Chifukwa chakuti Abele anapita kwa Mulungu mu njira ya Mulungu, Mulungu analandira msembe ya Abele.

-Kodi Mulungu anaganiza chiyani za Kayini ndi msembe yake?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:5

5-Koma Ambuye sanakondwere ndi Kayini ndipo sanalandire msembe yake. Chifukwa cha zimenezi, Kayini anali okwiya kwambiri ndipo nkhope yake yinali yakugwa ndiponso ya tsinya.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamukana kayini pamodzi ndi msembe yake.

-Kodi chifukwa chakuti Mulungu samakonda zipatso?
-Iyayi.

-Mulungu ndi amene analenga zipatso.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamukana Kayini pamodzi ndi msembe yake?

-Chifukwa chakuti Kayini sanamumvere Mulungu.
-Chifukwa chakuti Kayini sanabweretse nkhosa ngati msembe kwa Mulungu.

-Chifukwa chakuti Kayini amkayesa kupita kwa Mulungu mu njira yake, osakhala ya Mulungu.

-Kodi Kayini amkaganiza chiyani za iye?

-Kayini samkaganiza zakuti anabadwira mu tchimo.
-Kayini samkaganiza zakuti tchimo lake liyenera kulandira



4a-Koma nayenso Abele anabwera ndi mwana oyamba kubadwa wa imodzi mwa nkhosa zake, ndikuŵapereka ngati msembe.

-Abele anabweretsa nkhosa ngati msembe yake kwa Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Kayini ndi Abele anabweretsa msembe kwa Mulungu?

-Chifukwa chakuti Mulungu anamuwuza Kayini ndi Abele kuti abweretse msembe kwa Mulunguyo kuti afike kwa Iye.

-Kayini ndi Abele sanakatha kufika kwa Mulungu mu njira yawo.

-Kodi chifukwa chiyani Kayini ndi Abele sanakatha kufika kwa Mulungu mu njira yawo?

-Chifukwa chakuti anali ochimwa ndipo anasiyana ndi Mulungu.
-Chifukwa chakuti Mulungu amadana ndi tchimo ndipo Iye amapereka chilango kwa tchimo lililonse ndi imfa.

-Chifukwa chakuti Kayini ndi Abele sanakatha kupita kwa Mulungu, Mulungu anakhoza njira yakuti iwowo apitile kwa Iye.

-Kodi njira imene Mulungu anakhoza yakuti iwowo ipitire kwa Iye inali yotani?

-Mulungu anamulamula Kayini ndi Abele kuti apereke nkhosa ngati msembe.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulamula Kayini ndi

Abele kuti apereke nkhosa ngati msembe ?
-Mulungu amkafuna kumuphunzitsa Kayini ndi Abele.
-Kodi Mulungu amkafuna kumuphunzitsa chiyani Abele?

-Mulungu amkafuna kuti Kayini ndi Abele aŵawone magazi a nkhosa, ndipo adziwe kuti tchimo limabweretsa imfa.

-Mulungu amkafuna kuti Kayini ndi Abele awone magazi a nkhosa, ndipo adziwe kuti chilango cha tchimo ndi imfa.

-Kodi magazi a nkhosa anakatha kumupulumutsa Kayini ndi Abele?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani magazi a nkhosa sanakatha kumupulumutsa kayini ndi Abele?
-Chifukwa chakuti nkhosayo siyinalakwe.
-Chifukwa chakuti Kayini ndi aAbele ndi amene analakwa.

-Chifukwa chakuti magazi a nyama sangathe kulipira machimo a anthu.

-Mulungu amkamuphunzitsa Kayini ndi Abele kuti ndi Mulungu yekha amene angathe kuŵapulumutsa iwowo.

-Mulungu amkamuphunzitsa Kayini ndi Abele kuti angathe kufika kwa Mulunguyo mu njira ya Mulungu yekha.

-Kodi Mulungu anaganiza chiyani za msembe ya Abele?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 4:4b

4b-Tsopano Ambuye Mulungu anakondwera ndi Abele, nalandira msembe yake.



-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anakondwera ndi Abele ndikulandira msembe yake?

-Chifukwa chakuti Abele anamumvera Mulungu.

-Chifukwa chakuti Abele anabweretsa nkhosa ngati msembe kwa Mulungu.

-Chifukwa chakuti Abele anapita kwa Mulungu mu njira ya Mulungu.

-Kodi Abele amkadziwa chiyani za iye yekha?

-Abele anadziwa kuti anabadwira mu uchimo.
-Abele anadziwa kuti ayenera kulandila chilango cha imfa.

-Kodi Abele anadziwa chiyani za Mulungu?

-Abele anadziwa kuti Mulungu ndi oyera.
-Abele anadziwa kuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Abele anadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumupulumutsa iye.

-Abele anakhulupilira zakuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye ku machimo ake.

-Chomcho Abele anamumvera Mulungu ndikubweretsa nkhosa ngati msembe.

-Chifukwa chakuti Abele anamumvere Mulungu, Mulungu analandira msembe ya Abele.